May 2016

Wokondedwa wopembedzera,

Ndakhala ndikulingalira pa mafuso angapo pakatipa: Kuti kodi n'chifukwa chiyani timapemphela? Nanga kodi kwa inu pemphero ndi lophweka?

Pemphero silophweka, ndipo kupemphela mokweza kukhonza kubweletsa nkhawa kwa ena mwa ife. Komabe Mulungu ndi wokhulupilika po wasonkhanitsa amayi pamodzi mu nthawi ya mavuto ndi yosowa m'magulu a Project ya Hannah. Magulu athu a mapemphero amapereka malo otetezeka kuti anthu athe kufotokoza zomwe akukumana nazo.

M'modzi mwa amayi amene anatenga nao mbali ku msonkhano ku South Africa adathokoza Project ya Hannah chifukwa inamulimbikitsa kuti adzisonkhana pamodzi ndi amayi anzake lachisanu lirilonse ndi kupemphela. Iye adati, izi zinathandiza madela ambiri a moyo wake chifukwa ambiri mwa mapemphero ake anayankhidwa. Gulu lina la Project ya Hannah ku South Africa lakhala likupempha Mulungu kuti adzodze okhulupilira watsopano mu gulu lawo. Ndipo Amayi. S. akuyamika Mulungu kuti tsopano akuona. Iwo akuti anachititsidwa khungu ndi mizimu yoipa chifukwa amakhulupilila zikhalidwe za makolo awo. Iwo akhala akufuna kumapembedza Mulungu, koma amaphatikiza popembedza Mulungu ndi zikhulupililo za makolo. Akhristu ena anapita kunyumba kwawo ndi kukawapemphelela. Tikuthokoza Mulungu kuti tsopano akupembedza Mulungu wamoyo!

Tikayan'gana m'buku lopatulika muli madela ambili amene amatilimbikitsa ife moyo wa pemphelo.

- Pamenene tili amantha , pemphero limatithandiza kuti tipeze mtendele. "Musadere nkhawa konse; komatu m'zonse ndi pemphero, ndi pembedzero, pamodzi ndi chiyamiko, zopempha zanu zidziwike kwa Mulungu. Ndipo mtendere wa Mulungu wakupambana chidziwitso chonse, udzasunga mitima yanu ndi maganizo anu mwa Khristu" (Afilipi 4:6-7).

- "Idzani kuno kwa Ine nonsenu akulema ndi akuthodwa,ndipo Ine ndidzakupulumutsani inu"(Mateyu 11:28).

- "Yehova ali pafupi ndi iwo a mtima wosweka, Apulumutsa iwo a mzimu wolapadi"(Masalimo 34:18).

- Pemphero limatsekula maso athu kuti tithe kuona maiko "Anthu okodwere, napfuule mokodwera; Pakuti mudzaweruza anthu molunjika, Ndipo mudzalangiza anthu pa dziko lapansi Anthu akuyamikeni, Mulungu; Anthu onse akuyamikeni"(Masalmo 67:4-5).

Khalani nafe mwezi uno pamene tikupempherera alongo athu a kumwera kwa Afirika. "Kondwerere kumwamba, ndi dziko lapansi lisekere; anene mwa amitundu, Yehova achita ufumu!'(1 Chronicles 16:31).

Peggy Banks
Nkulu woyendetsa utumiki padziko lonse
Project ya Hannah

Tikulemekeza Mulungu chifukwa chotipatsa amayi olimbika mtima omwe anapita kumwera kwa Africa kukamema amayi anzathu kuti adzipemphera nafe ndi kumvera ma program a *Mai wa Chiyembekezo* m'ziyankhulo zawo zosiyanasiyana. Tipempherere kupezeka kwa zipangizo zothandizila ma bungwewa chifukwa amayiwa akuyesetsa kugwira ntchito molimbika kuti atukuke**.**

Werengani nkhani ziri mu'unsimu, zokhudza maulendo amene Project ya Hannah inachita posachedwapa, kukayambitsa magulu a mapemphero, komanso kuyendera nchito zimene zikuchitika kale maderawo.

**Swaziland:**

Wa mkulu oyendetsa utumiki ku Swaziland, Khaboe ,anapita ndi amayi okwana 16 ku dela la Kandida kuchokera ku Manzini. Ulendo okawayendela amayi ku Kandidawu anakonza ndi a Mfumu.

"Akazi a amfumu anatilandira bwino ndipo anathokoza chifukwa cha kupita kwathu pakuti iwo ali ku mudzi kutali ndi mizinda….. Tinawatengera sopo amene tinakawagawila amayiwa; sopo aliyense anali ndi chikalata cholembedwa mawu a Mulungu. Ndipo amayiwa anali osangalala polandila zithunzi"

Khaboe anagawana ndi amayiwa mawu a Mulungu, koma asanayambe kuwagawila mawu, anawafotokozela iwo za utumiki wa Project ya Hannah. Iwo anali okondwa kwambiri, makamamaka ndi ganizo loti iwo adzipempherelanso amayi anzawo pa dziko lonse la pansi. Tinanawaphunzitsanso zokhudzana ndi Dolika, mayi amene anadzipeleka pochita ntchito za zabwino ndi zachifundo powathandiza anthu a mzinda wa Yopa (Machitidwe Atumwi 9:36–43). Tizizipeleka powathandiza anthu ena ndi kawagawira osowa. Tinawalimbikitsa amayiwa kuti azichita zinthu zabwino ndikuwafikira anthu ena, makamaka osowa.

**South Africa:**

Mkulu woyan'ganira utumiki wa Project ya Hannah ku South Africa, Lyn Burnett, anapita kukayendera gulu la ku dera la KwaZulu Natal. Gululi linamufotokozera Lyn za program ya *Mai wa Chiyembekezo* ya m'chizulu imene ikukonzedwa ku TWR kumeneko.

Anafotokozanso mwa zina zochitika m'magulu awo a mapemphero, komanso magulu a omvera:

- Gulu la Umbumbulu la pafupifupi anthu 20, omwe ambiri mwa iwo ndi amayi amasiye omwe ali ndi chikhumbokhumbo chofuna kumudziwa ndi kupembedza Mulungu.
- Gulu la Kwanyswa linapeleka umboni wa mphamvu yokhudza sin'ganga wina wachizimayi yemwe anapeleka moyo wake kwa a Ambuye. Mphamvu ya Pemphero
- Gulu la m'bali mwa chigwa cha Valley Trust likupitilazabe kukhulupirira Mulungu. Miyoyo ya anthu m'gululi ikupitilala kusintha. Pamene amayi ena apeza ntchito, amachoka ndipereka mpata kuti amayi ena abwere.
- Gulu la Molweni liri ndi amayi ambiri amasiye omwe amamvera program m'chizulu komanso kupemphera limodzi.
- Gulu la mapemphero la Umlazi limakhala ndi mapemphero katatu tsiku lina lilonse.

Pamene Lyn anali kumeneko, anali ndi mwayi oyenda limodzi ndi Zoee komanso Philile kukakumana ndi gulu la mapemphero la Umlazi. Abusa Janet akhala akutsogolera gululi kuyambira chaka cha 1995. M'zaka za m'buyomu, akhala akugwiritsa ntchito makalendala a mapemphero a Project ya Hannah, ndi kukhala ndi chidwi kwambiri pa zopembedzera. Nthawi zambiri amakumana n'chisakasasa. Koma pamene kumabwera Lyn anakunga chihema, ndipo kunali amayi pafupi-fupi 20 ku msonkhanowu. Anali ndi nthawi yabwino yogawana mawu a Mulungu ndi kupemphera pamodzi

Tipemphere kuti kupezeka anthu oyendetsa utumiki ku Gauteng, KZN, ndi ku Cape Town. Tiyamike Mulungu chifukwa cha Verona, Avrille, Jay, Brenda, Eunice, Linda, Pumla, Ria, Margaret, Geraldine, komanso atsogoleri ena.